# CHIMWALIRA ZONE EXAMINATIONS BOARD

## 2023 PRIMARY SCHOOL ZONAL MOCK EXAMINATIONS

STANDARD 8

# CHICHEWA

[100 Marks]

Time Allowed: 2hours 15mins
01:00 – 03:15pm

Thursday, 23rd February

Name of a Learner________________________________________
(Surname First)
Name of School__________________________________________

## Malangizo:

1. Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi atatu.
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi: Gawo A, B, C ndi D.
3. Lembani dzina lanu ndi dzina la sukulu yanu pamwamba pa tsamba lino.
4. Lembani chimangirizo kapena kalata mu Gawo A ndipo muyankhe mafunso onse mu Gawo B,C ndi D.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6-10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21-25 | | | |
| 26- 30 | | | |
| 31-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| 41-45 | | | |

**CZEB**

**GAWO A (MALIKSI 30)**

**Langizo:**

- Yankhani funso limodzi mwa mafunso awiri alim'musiwa
- Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata
- Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 asaposere150.

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu woti "**KUSAMALIRA NTHAKA**". Mwa zina tsatani izi polemba chimangirizo chanu:

**Ndime yoyamba:**
- Kufunika kwa nthaka.
- M'mene anthu amaonongera nthaka.

**Ndime yachiwiri:**
- Mavuto omwe akudza chifukwa choononga nthaka
- Mmene tingasamalire nthaka

**Ndime yachitatu:**
- Ubwino osamala nthaka.
- Magulu ndi mabungwe omwe akuthandizirapo kusamalira nthaka

**Kapena**

2.Lembani kalata kwa phungu wa nyumba ya malamulo woyimira dera lanu kuti akupemphereni ku boma msewu waphula m'dera lanu. Mwa zina polemba tsatarani izi:

**Ndime yoyamba**
- Dzina la msewu
- Kumene msewu ukupita
- Kutalika kwa msewu

**Ndime yachiwiri:**
- M'mene msewuwo ulili panopa
- Mavuto amene akuchitika chifukwa cha msewuwo
- Zomwe boma lingachite pa vuto la msewuwo

**Ndimeyachitatu**

.Kuthandiza kwa msewu ukazakonzedwa

GAWO B

3. Kumvetsa Nkhani

**Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yakhani mafunso otsatirawo**

Kalekale mdziko la Fukizi mudali mfumu yotchedwa Mbanira. Mfumuyi idali yolemera kwambiri. Mfumu Mbanira idali ndi ana awiri. Wachisamba adali Tepatepa ndipo winayo adali Ganiza. Mfumu Mbanira idali ndi zifuyo zochuluka monga:ng'ombe, nkhuku, mbuzi, abakha ndi nkhunda.Pakhomo pawo padali pa mwanaalilenje.Ponena mwatchutchutchu mfumuyi idali mpondamatiki.Mwadzidzidzi mfumu Mbanira idadwala koopsa ndipo idayitanitsa ana ake aja kuti ikambe nawo. Iyo idapempha ana aja kuti aliyense anene zokhumba zake iyo ikadali ndi moyo.

Tepatepa adali woyamba kunena za khumbo lake lotenga chuma chonse cha atate ake.Ganiza adanena zakhumbo lake lomwe lidali lakuti atate akewo achire. Mfumu ija itamva zokhumba za ana ake aja idapereka ndodo imodzi kwa mwana aliyense ndipo idawauza anawo kuti akasungitsitse ndodo zija.Madzulo atsikulo Tepatepa adavutika mu mtima.

Adatenga ndodo yake ija nayithyola ndi kuiponya pa moto.Iye adawadandaula atate ake pomupatsa ndodo m'malo mwa chuma.M'mawa kutacha mfumu Mbanira idayitanitsa nduna zake zonse, mikoko yogona, achibale, mkazi ndi ana ake. Iyo idawuza anthuwo kuti ikufuna igawiretu chuma chake kwa ana ake kuti asadzalimbane patsogolo.Mfumu idawuza mwana wake Tepatepa kuti atenge ndodo yake ndi kuloza chomwe akufuna. Apatu Tepatepa adangoti kakasi. Iye adayamba kulira nalowa mnyumba mwake. Mfumu itamva zomwe Tepatepa adachita ndi ndodo yake ija idawuza Ganizani kuti atenge ndodo yake ndi kuloza zomwe akufuna.Ganiza adatenga ndodo yake ndipo adaloza chuma chonse pamodzi ndi atate ake. Pamenepatu mfumu Mbanira idauza Ganiza kuti chuma chonse chomwe waloza chidzakhala chake komanso poti waloza iye mfumu,ufumunso udzakhala wake.Iyo idatsamira mkono. Anthu adawombam'manja ndipo nthungululu zidamveka ponseponse.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pamizere ili pansi pa funso lililonse.**

a. Kodi mfumu Mbanira imakhala kuti?

______________________________ (malikisi 1)

b. N'chifukwa chiyani mfumuyi idayitanitsa ana ake.

______________________________

______________________________ (malikisi 2)

c. Pezani mawu mnkhaniyi omwe ali ndi matanthauzo ofanana ndi awa

i. Ziweto

______________________________ (malikisi 1)

ii. Akulu akale

______________________________ (malikisi 1)

iii. Woyamba kubadwa m'banja

______________________________ ______________________________ (malikisi 1)

d. N’chifukwa chiyani Tepatepa adalephera kulandira chuma kuchokera kwa atate ake.

______________________________________________

______________________________________________ (malikisi 2)

e. Tchulani ziweto ziwiri zomwe Ganiza adaloza

______________________________________________

______________________________________________ (malikisi 2)

f. Tepatepa adathyola ndodo ija chifukwa chiyani?

______________________________________________ (malikisi 2)

g. Perekani matanthauzo a mawu awa

i. Mpondamatiki

______________________________________________(malikisi 1)

ii. Adangoti kakasi

______________________________________________(malikisi 1)

h. N’chifukwa chiyani kudamveka nthungululu m’mudzi muja?

______________________________________________

______________________________________________ (malikisi 2)

i. Lembani mutu wa nkhaniyi

______________________________________________ (malikisi 2)

j. Cholinga cha mfumu chidali chiyani poitanitsa akuluakulu pogawa chuma

______________________________________________ (malikisi 2)

**GAWO C (malikisi 10)**

**4. Werengani ka nkhani kali musika ndipo muyankhe mafunso otsatirawa**

A Najere: Zikomo! Zikomo!

A Banda: Eee! Tikuwopeni?

A Najere: Ayi musatiwope. Kungoti kunyumbaku akwatira mkazi wina. Zimenezi zandidandaulitsa ndi momwe kunjaku kwaopsera ndi matenda a Edzi.

Mafunso

a. i. Kodi ndi malonje anji omwe mwawerengawa?

______________________________________________ (malikisi 1)

ii. Kodi pa malonjewa a Banda ndi ndani?

______________________________________________ (malikisi 1)

b. Tchulani njira imodzi yopewera Covid 19 ku sukulu.

______________________________________________(malikisi 1)

c. Ndi chifukwa chiyani ndalama yoperekera uthenga wa maliro imakhala yochepa.

______________________________________________

______________________________________________(malikisi 2)

**5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:**

a) chizimalupsa

______________________________________________(malikisi 1)



b) bwino

______________________________________________________________________________(malikisi 1)

c) chembeza

______________________________________________________________________________(malikisi 1)

d) ulesi

______________________________________________________________________________(malikisi 1)

e) phati

______________________________________________________________________________(malikisi 1)

GAWO D (makilisi 40)

**Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapena D) m'mafunso otsatirawo**

**Mafunso 6 mpaka 10: Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.**

6. Awo atenga mabuku anga.
A mfotokozi B mlowam'malo
C mneni D mperekezi

7. Galu wadya matemba onse.
A mperekezi B muonjezi
C mfotokozi D dzina

8. Anawa achita dala kutaya madziwa.
A dzina B mfotokozi
C mperekezi D muonjezi

9. Ndipatseni ichi osati icho.
A mlowam'malo B muonjezi
C mneni D mvekero

10. Mbale zonse zili pa thandala.
A mlumikizi B mperekezi
C muonjezi D mvekero

**Mafunso 11 mpaka 15; Sankhani matanthauzo a mikuluwiko.**

11. Chikumbutsa nkhwangwa n'chisanu.
A zinthu zina zimafuniko panthawi yake
B ntchito zimafunika kuthandindizana
C zinthu zina zimafunika nthawi zonse
D ntchito zina zimafunika kugwira utakonzeka

12. Khoswe akakhala pa mkhate sapheka
A mulandu ukakhalitsa umavuta kuweruza
B mlandu wa mbale umavuta kuweruza
C mlandu wa amfumu umaweruzidwa bwino
D mlandu ukhala wako umaweruzidwa bwino

13. Kuwongala mtengo mpoyamba.
A kudula mtengo usanakule kumakhala bwino
B kukoza tsogolo ndi bwino kwambiri
C ndibwino kukoza zinthu zisanalakwike
D ndibwino kusamalira mtengo

14. Mapanga awiri avumbwitsa.
A kuchita zinthu zambiri kumapindulitsa
B kuchita zinthu mofananitsa sikupindulitsa
C kuchita zinthu ziwiri pakamodzi umapambana
D kuchita zinthu ziwiri nthawi imodzi sikupindulitsa

15. Fodya wako ndi uyu ali pamphuno wapachala ndi wapanphepo.
A kudalira zinthu zomwe zili zako
B kudalira zinthu za mnzako
C kudalira zinthu zobwereka
D kudalira zinthu zopatsidwa

**Mafunso 16 mpaka 20: Sankhani nthambi za chaganizo.**

16. Sindikusiya mpaka undidalitsa.
A ya muonjezi B ya dzina
C ya mfotokozi D yoyima payokha

17. Sizoona kuti chaka chino kuli chilala.
A ya mfotokozi B ya dzina
C yoyima payokha D ya muonjezi

18. Zoti amayi abweranso sizikudziwika
A ya mfotokozi B ya muonjezi
C yoyima payokha D ya dzina

19. Madalo watenga nsalu imene anamugulira
A ya muonjezi B ya dzina
C yoyima payokha D ya mfotokozi

20. Ngakhale wabwera kwathu sindikupatsandalama zako.
A ya dzina B ya mfotokozi
C yoyima payokha D ya muonjezi

**Mafunso 21 mpaka 25: Sankhani mimvekero**

21. Wafika mbandakucha kuli_________
A mbu B psu
C bii D mbee

22. Pa mudzi panali ___________
A phe B mbwe
C zii D ndwi

23. Buluzi anali ___________ kukhoma.
A chete B khuma
C myaa D phati

24. Mbavayo inangoti ________ kusowa chonena.
A yasa B phi
C jenkha D zi

25. Kambuku anangoti ______ watulukira.
A deru B balamanthu
C mbwe D fwanthu

**Mafunso 26 mpaka 30: Sankhani mitundu ya aonjezi**.

26. Amalume avulala kwambiri pangoziyo.
A wanthawi B wamuyeso
C wowerenga D wamchitidwe

27. Masiku ano kuli ana amwano.
A wa malo B wanthawi
C wa mchitidwe D wa muyeso

28. Tonse tinafika bwino.
A wa malo B wopenekera
C wamchitidwe D wamuyeso

29. Buluzi ali gone pamwala.
A wa malo B wamchitidwe
C wanthawi D wamuyeso

30. Inde sindipita nawo kumudziko.
A wopeneka B wokana
C wovomera D wamchitidwe

**Mafunso 31 mpaka 35: Sankhani kachitidwe ka aneni.**

31. Abambo adula mtengo.
A kachitidwe kawochita
B kachitidwe ka wochitidwa poyera
C kachitidwe ka wochitidwa monyazitsa
D kachitidwe ka wochitidwa mchibisira

32. Mbuzi yagundidwa ndi galimoto.
A kachitidwe ka wochita
B kachitidwe kawochidwa mchibisira
C kachitidwe ka wochitidwa poyera
D kachitidwe ka wochitidwa monyazitsa

33. Mbewa zapheka lero
A kachitidwe ka wochitidwa poyera
B kachitidwe ka wochitidwa monyazitsa
C kachitidwe kawochitidwa mchibisira
D kachitidwe kawochita

34. Ane wavumbwa ndi mvula.
A kawochitidwa poyera
B kachitidwe kawochita
C kachitidwe kawochitidwa monyazitsa
D kachitidwe kawochitidwa mchibisira

35. Agogo apha mbuzi.
A kachitidwe kawochita
B kachitidwe kawochitidwa poyera
C kachitidwe kawochitidwa mchibisira
D kachitidwe kawochitidwa manyazitsa

**Mafunso 36 mpaka 40: Ntchito za "ndi"**

36. Amayi aphika nsima ya ndi lero.
A .ngati mneni
B. ngati mperekezi
C. ngati mvekero
D. ngati mlumikizi

37. Ine ndipita lero kumudzi.
A. ngati mneni
B ngati mvekero
C ngati mperekezi
D ngati mlowam'malo

38. Nyumba yake ndi yatsopano.
A. ngati mneni B. ngati mperekezi
C ngati mlowam'malo D.ngati mlumikizi

39. Apite ndi ine.
A ngati mlumikizi
B ngati mperekezi
C ngati mlowam'malo
D ngati mvekero

40. Abambo ndi mayi adwala.
A ngati mlowam'malo
B ngati mperekezi
C ngati mlumikizi
D ngati mvekero

**Mafunso 41 mpaka 45: magulu a mayina**

41. Chimanga changa chabedwa.
A Li –; Ma- B Chi –; Zi-
C I –; Zi- D Ka –; Ti-

42. Mwana wake wapezeka kumunda.
A .Ku + mneni B. I –; Zi-
C. Ku –; Pa –; Mu- D. U –; Ma-

43. Sukulu yathu ndi ya ukhondo.
A. U –; Ma- B Chi –; Zi-
C. I –; Zi- D Li –; Ma-

44. Madzi akatayika sawoleka.
A. I –; Zi- B. Ku –; Pa –; Mu-
C. U –; Ma- D. Li –; Ma-

45. Khasu lake lathyoka mpini.
A. I –; Zi- B. U –; Ma-
C. Li –; Ma- D. Mu –; Mi-

# MAFUNSO ATHERA APA